




CHIKHULUPIIRO CHA MIZIMU CHIULULIKA

Phunziro 10, June 8, 2024




"Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mfuu, ndi mau a mngelo wamkulu, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Khristu adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse."
(1 Thessalonians 4:16, 17)

Bodza loyamba limene Mdyerekezi anatiuza linali: “Kufa simudzafai” (Genesis 3:4). Ndipo ife tinazikhulupirira zimenezi!

Pafupifupi anthu onse anakhulupirira - ndipo akupitirizabe kukhulupirira - kuti tili ndi mzimu mwaife omwe siufa, kapena mwanjira ina, tili ndi mbali ina ya moyo wathu imene imapulumuka ku imfa.

M’malo mwake, Baibulo limafotokoza momveka bwino komanso motsindika: “Moyo wochimwawo ndiwo udzafa” (Ezekiel 18:20). Mkangano waukulu wa miyamba umazungulira pa funso lofunika kwambiri: Kodi mudzakhulupirira ndani, mdierekezi kapena Mulungu?



Chikhulupiliro cha mizimu komanso imfa:



Mzimu wosafa.



Imfa mu Chipangano Chakale.



Imfa mu Chipangano Chatsopano.



Chikhulupiliro cha mizimu m’masiku otsiridza:



Zizindikiro komanso zodabwitsa.



Cholinga cha chikhulupiliro cha mizimu.

A group of people is shown from behind, looking towards a large, glowing silhouette of a person in the background. The scene is dimly lit, with a warm, golden glow emanating from the silhouette. The people in the foreground are mostly in shadow, with some highlights on their hair and shoulders. The overall atmosphere is one of anticipation or a significant moment.

CHIKHULUPIIRO

CHA MIZIMU

KOMANSO IMFA



MOYO WOSAFA

“Monga mtambo umazimirira ndi kukanganuka, momwemonso munthu amene walowa m’manda sabwerera.” (Yobu 7:9 CCL)

Kawirikawiri, zimakhulupiridwa kuti munthu ali ndi mbali ziwiri za chilengedwe chake: thupi ndi mzimu (kapena moyo). Zimakhulupiridwanso kuti magawo awiriwa akhoza kukhala ndi moyo paokhapaokha.

Koma Baibulo limaphunzitsa kuti tinapangidwa mu “zigawo” zitatu: “mzimu, moyo, ndi thupi” (1 Atesalonika 5:23). Limaphunzitsanso kuti zigawo zimenezi zimadalirana. Genesis 2:7 limatiphunzitsa kuti Mulungu analenga thupi, nkuikamo mpweya (mzimu), ndipo linakhala munthu wamoyo (“munthu wamoyo,” mu Chihebri, ndi nefesh = “moyo”).

Choncho, munthu wamoyo ndiko kuphatikizana kwa thupi ndi mzimu. NDIFE moyo, ife simzimu paokha.

Pamene mpweya wamoyo utichokera ife, sitikhalanso amoyo. Palibe gawo liri lonse la umunthu wathu lomwe limazindikira pamene imfa yafika. Thupi limafa, mzimu (mphamvu ya moyo) umabwerera kwa Woupereka, ndipo mzimu, womwe umachokera mugwirizano wa thupi ndi mzimu, sukhalanso wa moyo (Mlaliki 12:1-7; Ezekiel 18:20; Yobu 7 :7-9).



THUPI



MZIMU



MOYO

MOYO WOSAFA

“Monga mtambo umazimirira ndi kukanganuka, momwemonso munthu amene walowa m’manda sabwerera.” (Yobu 7:9 CCL)



Kuyambira pamene uchimo unalowa pa dziko lathu lapansi, Satana wakhala akugwiritsa ntchito anthu amene amafuna kulankhulana ndi anthu akufa ndi kupeza chidziwitso chapadera chonena za zinthu za tsopano lino kapena zamtsogolo kuchokera kwa iwo.

Anthu amtundu uwu, omwe amagwiritsanso ntchito njira zina monga kubwebweta, matsenga ndi kukhulupirira nyenyezi, masiku ano amadziwika kuti okhulupilira mizimu.



Baibulo limaphunzitsa kuti “aliyense wakuchita izi Yehova anyansidwa naye” (Deuteronomo 18:10-12). Chilango cha mlandu uwu chinali imfa (Levitiko 20:27).

“Ndipo pamene iwo adzati kwa iwe, Funa kwa olaula, ndi obwebweta, amene alira pyepye, nang'ung'udza; kodi anthu sadzafuna kwa Mulungu wao? Chifukwa cha amoyo, kodi adzafuna kwa akufa? Kuchilamulo ndi kuumboni! Ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndithu sadzaona mbandakucha” (Yesaya 8:19-20).



IMFA MU CHIPANGANO CHAKALE

"Akufa salemekeza Yehova, kapena aliyense wakutsikira kuli chete" (Masalimo 115:17)



Ngakhale kuti palibe amene amanena pa maliro kuti "m'bale wathuyu akupita molunjika ku gehena," maumboni ambiri amaphunzitsa kuti, pamene imfa yabwera, "abwino" amakwera molunjika Kumwamba kukakhala ndi Yesu, ndipo "oipa" amalangidwa kapena kumangoyendayenda. Koma kodi Baibulo limaphunzitsa chiyani pa nkhaniyi?

Kodi tikamwalira tingatamande Mulungu?

Masalimo 115:17

Kodi amene anamwalira amadziwa zimene zimachitikira achibale awo kapena anzawo?

Yobu 14:21

Kodi akufa angalumikizane ndi amoyo?

Mlaliki 9:6

Kodi tingapitirize kuganiza tikamwalira?

Mlaliki 9:5

Kodi tidzatha kupitiriza kuchita chilichonse tikadzafa?

Mlaliki 9:10

Chipangano Chakale chimaphunzitsa kuti imfa ndi maloto. Kugona ndi kudzuka pamene Mulungu atiitana kukhalanso ndi moyo (1 Mafumu 2:10; 14:20; Danieli 12:13).



IMFA MU CHIPANGANO CHATSOPANO

“Bwenzi lathu Lazaro wagona tulo; koma Ine ndikupita kumeneko kukamudzutsa” (Yohane 11:11)

Chipangano Chatsopano chimaphunzitsa, mofanana ndi Chakale, kuti imfa ndi tulo tomwe Yesu yekha ndi amene angatidzutseko (Yohane 11:11-14; Yohane 5:28-29).

Mukalata yake yopita kwa Atesalonika, Paulo analankhula nawo zokhuza “iwo akugona,” kutanthauza kuti amene anali atamwalira kale, ndipo anawauza kuti adzaukitsidwa ndikupita ndi Yesu pa Kubwera kwake Kwachiwiri (1 Atesalonika 4:13-18). Paulo akanakhala kuti akakhulupirira kuti okhulupirira amapita kwa Yesu akangomwalira, akanawauza zimenezi m’ malo mwa zomwe ananena.



Polankhula za akufa, Paulo ananena kuti adzakhala ndi moyo “pamene Khristu adzabwera,” osati asanabwere (1 Akorinto 15:22-24). Iye amatiuzanso kuti “si tonse tidzagona.” Amoyo adzasandulika mukamphindi, koma akufa adzauka ali osandulika kale (1 Akorinto 15:51-52).

Chiukitso ndicho chinsinsi cha kukhala mwa Yesu. Popanda chiukutso, palibe chipulumutso (1Akorinto 15:13-18). Muchiukitso ndimomwe tidzalandire cholowa chathu, chotero tiyenera kuyembekezera nthawi imeneyo (1 Petro 1:3-5).

**CHIKHULUPIIRO
CHA MIZIMU
M'MASIKU
OTSIRIDZA**



ZIZINDIKIRO KOMANSO ZODABWITSA

pakuti adzauka Akhristu onyenga ndi aneneri onyenga, ndipo adzachita zizindikiro ndi zozizwitsa, kuti akasoheretse, ngati nkutheka, osankhidwa omwe.” (Marko 13:22)

Chikhulupiliro cha mizimu ndi gulu lochita chimodzi lotsogozedwa ndi satana, ndipo maziko ake ndi kusafa kwa mzimu. Otsatira ake amakhulupirira kuti angathe kulankhula ndi akufa, ndipo amanena kuti amalandira mphamvu zawo zauzimu kuchokera kwa iwo.

Ngakhale kuti pakadali pano, Mulungu anaika malire pazomwe angathe kuchita, nthawi idzafika pamene Iye adzawalola kuchita zozizwitsa zawo mwaufulu zimene zidzadabwitsa onse owaona (Marko 13:22; 2 Atesalonika 2:9; Chivimbulutso 7:1 ; 13:13-14).

Titaona kubwezeretsedwa kwathunthu kwa munthu wodwala matenda osachiritsika; Galimoto itaimitsidwa kuti isatigunde; kapena amayi athu okondedwa, amene anamwalira, akulankhula nafe mokoma mtima pamaso pathu kodi tidzakwanitsa osakhulupirira amene akuchita zodabwitsa zoterozo? Sitidzatha kudalira mphamvu zathu kapena malingaliro athu.



Tidzatetezedwa kudzera pa zimene timadziwa kuchokera m’Mawu a Mulungu okha, komanso kukhulupirira Yesu kotheratu, ndi kumene kudzatithandiza kukana mayeso omalizira a mdani (Yesaya 8:20; Aefeso 6:13).

CHOLINGA CHA CHIKHULUPIIRO CHA MIZIMU

“Imeneyi ndiyo mizimu ya ziwanda imene imachita zizindikiro zodabwitsa ndipo imatuluka kupita kwa mafumu a dziko lonse, kukawasonkhanitsa ku nkondo ya pa tsiku lalikulu la Mulungu Wamphamvuzonse” (Chivumbulutso 16:14)

Cholinga cha Satana ndichakuti apambane pankhondo yolimbana ndi Mulungu, kugwetsa boma lake, ndi kukhala pampando wake wachifumu (Yesaya 14:13-14). Kuti achite zimenezi, adzagwiritsa ntchito njira iliyonse kuti akope aliyense, kuyambira maulamuliro andale amene amatilamulira (Chivumbulutso 16:12-14).

“Pachimake pazochitika za mkangano waukulu mu chinyengo chachikulu, Satana mwini adzaziyerekeza monga Kristu” (EGW “The Great Controversy”, Chapter 39 p. 625.)



Koma idzakhala nthawi imeneyi pamene Yesu adzathetse nkhaniyi (Chivumbulutso 16:15). Satana ndi mdani wogonjetsedwa. Anagonjetsedwa ndi Khristu, komanso kugonjetsedwa ndi omwe akakamira pa mwazi wake (1 Yehone 2:14; 4:3-4; Chivumbulutso 3:21; 5:5; 12:11).

Chizindikiro chapaderadera cha omwe amatsutsana ndi bodza lokhulupilira mizimu ndi : “kusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu” (Chivumbulutso 14:12).

“Ndinaona kuti oyera mtima ayenera kumvetsetsa bwino choonadi chimene alinacho, chimene ayenera kutsatira kuchokera mu Malemba. Ayenera kuzindikira mmene akufa amakhalira; pakuti mizimu ya ziwanda idzaonekeranso kwa iwo, monga achibale awo okondedwa, kapena abwenzi awo, amene adzalalikira kwa iwo ziphunzitso zosagwirizana ndi malemba. Adzachita zonse zomwe angathe kuti akhale akumvera ena chisoni ndipo adzachita zozizwitsa pamaso pawo kuti atsimikizire zomwe akulalikirazo. Anthu a Mulungu ayenera kukhala okonzeka kulimbana ndi mizimu imeneyi kudzera mu choonadi cha Baibulo chakuti akufa sadziwa kalikonse, ndiponso kuti amene amaoneka choncho ndi mizimu ya ziwanda.”

EGW (Early writings, p. 262)